

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitsa kuchokera m'Baibulo kupita kwa amene akulalikira Uthenga Wabwino

CHOSASINTHA MKATI MWA MLIRI WA COVID-19

Matenda a COVID-19 amene amayambitsidwa ndi kachikolombo kotchedwa coronavirus, anayamba ku Wuhan ku China mu November 2019. Kuchokera nthawi imeneyo, kachikolomboka kafala mofulumira ndipo kagwira anthu osiyanasiyana padziko lonse lapansi. Pamene tikulemba kalatayi, pali anthu miyandamiyanda amene apezeka ndi nthendayi ndipo enanso mazanamazana amwalira kale. Tsiku lililonse anthu ochuluka akumapezeka ndi nthendayi ndipo tikuyembekeza kuti pakhala kukwera kwa chiwerengero cha iwo amene apezeka ndi kachilomboka komanso amene amwalire ndi nthendayi.

Pofuna kuchepetsa kufala kwa kachilomboka, maiko ambiri pa dziko lapansi alamula kuti mabizinezi atsekedwe kaye ndipo misonkhano isachitikenso. Mizinda yambiri ikumauza nzika zake kuti zisatuluke m'nyumba zao pokhapokha ngati akupita kukagula zakudya ndi kuchita zinthu zina zimene zili zofunikira kwambiri. Zimenezi zapangitsa kuti chuma cha dziko chibwerere pambuyo ndipo anthu ambiri achotsedwa ntchito komanso alibe podalira. Kukumana kwa anthu kwachepetsedwa kwambiri, ndipo ngakhale nyumba zambiri zopempherera

zatskedwa potsatira lamulo la boma. Moyo wa tsiku ndi tsiku monga m'mene timaudziwira wasinthiratu m'njira zambiri. Imeneyi ndi nthawi yofunsa mafunso ambiri komanso yochititsa mantha.

Nthawi zonse m'moyo uno pamakhala zinthu zimene zimasintha komanso zimene sitiziyembekezero, komabe ulendo uno zinthu zake zikusintha mwachangu kwambiri padziko lonse, ndipo tsopano tikudziwa kwambiri za zinthu izi zosakhazikika—

moyo, imfa, thanzi, kupembedza, maubale, ntchito, kupuma ntchito, komanso ngakhale zinthu zofunikira pa moyo monga madzi ndi chakudya.

Zinthu izi zosakhazikika zili gawo la moyo, koma kutengera pa chisokonezo chimene

chikuchitika, chinthu chimodzi chokha chili chokhazikika ndipo sichisintha—Mulungu. “Pakuti Ine Yehova sindisinthika” (Malaki 3:6). Chikondi ndi chisamaliro chake kwa anthu ake zili zosasinthika. Iye akhalabe kothawirako kwathu m'nthawi ya msautso komanso wotipatsa chakudya pa tsiku la njala. Anthu ambiri akuvutika ndi mantha komanso kusowa chiyembekezo. Tamvera Mwana wa Mulunguwe, ngakhale kuti ukhoza kukhala mkati mwa masiku amene sukudziwa kuti zitithera bwanji, kumbukira kuti ifeyo ndife ongodutsa ndi alendo chabe m'moyo uno. Tsiku lililonse tikhoza kukhulupirira mwa Iye wosasintha kuti atitsogolera ndipo tikafika bwino ku chigonjetso chazimu mwamtendere.

Woimba wina anaimba kuti, “Mulungu anati, ‘Inuyo mudzapambana!’” —mws



CHITANI ZISANU IZI



THANDIZANI KUTHETSA CORONAVIRUS

1. **Manja** Musambe pafupipafupi.
2. **Mkono** Mukhosomolere m'menemo.
3. **Nkhope** Musaikhudze.
4. **Pokhala** Mutalikirane ndi ena.
5. **Kunyumba** Khalani m'menemo.

World Health Organization

Zitsanzo za umulungu za unzika wabwino
2
Mau a Mkonzi
3

Zokhudzana ndi mliriwu; Chithonhozo mu malonjezano; Mu nthawi ngati izi
4

Dzukani ndi kupemphera 5
Kodi chikhulupiriro chathu chili kuti
6

Magorimisabibu— choopsa pakati pako; Inu muli mchere wa dziko lapansi
7

Kutalikana/ Kulumikizana
Zovala zopindidwa
8

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

ZITSANZO ZA UMULUNGU ZA UNZIKA WABWINO

Maboma ndi maiko ambiri apempha kapena alengeza kuti pasakhalenso kukumana kwa anthu ngati gulu panthawi iyi imene dziko latekeseka chifukwa cha kachilomboka. Funso limene ambiri akhala akutsutsana ndilo lakuti, kodi ifeyo ngati Akhristu tikuyenera kutsata ndondomeko zimenezi ndipo tisamasonkhane pa nthawi yathu yoikika imene timapemphera kapena mwina tisamvere lamulo la munthu ndipo tikapembedze Mulungu mu matchalitchi athu? Pokhala gulu la okhulupirira, kodi tikatero tipereka chitsanzo chotani kapena uthenga wotani kudzikira ndi anthu okhala nawo limodzi, ngati atatiwona titasonkhana pamodzi ndi kupembedza mosutsana ndi lamulo la boma. Kodi zimenezi zidzaonetsa kuti ndife odzipereka kwathunthu potumikira Mulungu kapena kuti tili ndi mtima wosamvera ndi wogalukira?

Petro, pamene analetsedwa kulalikira uthenga wabwino ndi akulu a Ayuda anawayankha nati, “Tiyenera kumvera Mulungu koposa anthu” (Machitidwe 5:29). Pa Ahebri 10:25 timawerenga kuti, “Osaleka kusonkhana kwathu pamodzi, monga amachita ena.” Komanso mbali ina Yesu anaphunzitsa M'malemba osiyanasiyana kuti tikuyenera kugonjera iwo amene ali pa ulamuliro. Paulo, ponena za maboma pa Aroma 13:1 anati, “Anthu onse amvere maulamuliro a akulu; pakuti palibe ulamuliro wina koma wochokera kwa Mulungu; ndipo iwo amene alipo aikidwa ndi Mulungu.”

Malemba amaphunzitsa momveka bwino kuti Akhristu akuyenera kukhala nzika zabwino komanso atsature malamulo ndi zonena za boma; ndipo izi sizitengera ngati mukugwirizana nazo kapena ayi. Koma ngati boma likhoza kuletsa kulalikira kwa uthenga wabwino, pofuna kuletsa uthenga wabwino monga m'mene zinaliri mu nthawi ya Petro, Akhristuwo asamvere lamulo la bomalo. Momveka bwino, sizili choncho ndi corona virus kapena chimene chikupangitsa kuti maboma adzilamula kuti mizinda yambiri itseke malo opempherera kwa kanthawi. Imeneyi ndi nkhani yokonda mnansi wathu mwakuti sitikufuna kufalitsa kachilomboka.

Akhristu ali ndi udindo womvera lamulo lakanthawi loikidwa ndi munthu mu nyengo ino ya msautso ndipo agwiritse ntchito njira zina zonse zopemphera ngati gulu kudzera mu zipangizo zamakono zotumizira mauthenga monga mafoni pofuna kulumikizana ndi abale komanso alongo mwa Ambuye. Petro anaimaliza bwino nkhaninyi pa 1 Petro 2:13-17 pamene anati: “Tadzigonjani kwa zoikika zonse za anthu, chifukwa cha Ambuye; ngakhale kwa mfumu, monga mutu wa onse kapena kwa akazembe....Pakuti chifuniro cha Mulungu chitere, kuti ndi kuchita zabwino mukatontholetse chipulukiro cha anthu opusa monga mfulu, koma osakhala nao ufulu monga chobisira choipa, koma ngati akapolo a Mulungu. Chitirani ulemu anthu onse. Kondani abale. Opani Mulungu, Chitirani mfumu ulemu.” —mws

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kutu mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani. —Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi (Kalata Yapadera)



Adzatisiyanitsa ndani ndi chikondi cha Khristu? Nsautso kodi, kapena kupsinjika mtima, kapena kuzunza, kapena njala, kapena usiwa, kapena zoopsa kapena lupanga kodi?...Koma m'zonsezi, ife tilakatu, mwa Iye amene anatikonda.

Pakuti ndakopeka mtima kuti ngakhale imfa, ngakhale moyo, ngakhale angelo, ngakhale maufumu, ngakhale zinthu zilipo, ngakhale zinthu zilinkudza, ngakhale zimphamvu, ngakhale utali, ngakhale kuya, ngakhale cholengedwa china chilichonse, sichingadzakhoze kutsiyanitsa ife ndi chikondi cha Mulungu,

chimene chili mwa Khristu Yesu Ambuye wathu. —Aroma 8:35-39

Taonani chitonthozo ndi chitsimikizo chimene chilipo podziwa kuti palibe chimene chingathe kutilekanitsa ife ndi chikondi cha Mulungu. Zovuta zidzabwera ndithu, koma palibe mphamvu, kachilombo kapena kuchotsedwa ntchito zimene zikhoza kulanda chipulumutso kuchokera kwa mwana wa Mulungu. Pali nangula wa chiyembekezo mwa Khristu ndiponso tsogolo lowala lamuyaya likudikirira ngati tikhala okhulupirika kwa Ambuye ndi Mulungu wathu.

Ulendo uno Ambuye ananditsogolera kuti ndisindikize kalata yapadera ya Uthenga wa Choonadi imene ili yosiyaniirako ndi makalata ena onse. Dziko lathu lili mu nsautso chifukwa cha kufala kwa matenda a COVID-19, ndipo oyera mtima a Mulungu akukumana ndi zinthu zambiri zimene sakudziwa kuti ziwathera bwanji. M'dzikoli pali mantha komanso mafunso ochuluka, ndipo mwana wa Mulungu akhoza kukhala ndi mtendere waukulu podziwa kuti Mulungu ali pampando wa ulamuliro. Ngakhale sitingathe kupeza mayankho ku funso lililonse pa za chifukwa komanso cholinga cha zonse zimene zikuchitika m'moyo uno, tikudziwa kuti Mulungu adzakonza kuti zonse zichitire ubwino mizimu ya anthu. Kalata uyu wapadera ndi msonkhamsonkha wa mauthenga osiyanasiyana amene alembedwa ndi iwo amene ali atumiki osiyanasiyana a mpingo wa Church of God kuchokera ku dziko lonse lapansi kuti amangirire, alimbikitse ndi kutonthoza oyera mtima a Mulungu pamene akudutsa mu nyengo iyi yosautsa. Ndikukhulupira kuti kalatayi ikhala mdalitso wapadera ndi chilimbikitso kwa anthu a Mulungu.,

Pamene anthu ena ali kakasi ndipo asokonezeka, ndikufuna kukulimbikitsani kuti muike chikhulupiriro chanu mwa Ambuye Yesu ndipo mukhala mwabata ndi mopanda nkhawa pamene mukupitirira kuyenda naye. Mu nthawi yamavuto ngati iyi, kaya mukhala ndi moyo kapena mufa, komabe pali mtendere wina wapaderadera umene umaposa chidziwitso chonse. Ngati simunapulumsidwe ku uchimo, imeneyi ndi nthawi ya mtengo wapatali yakuti mulape ndi kulandira mpatso ya chipulumutso. Ngati muli ndi nkhawa kapena mukuchita mantha, dziwani kuti Mulungu amakuganizirani koposa. Mzimu Woyera anaperekedwa ngati mtonthozi kuti atitonthoze ndi kukhazikitsa pansu mizimu yathu ngakhale tikumane ndi anamondwe m'moyo uno.

Dziko lapansili lakumana ndi zokhoma zambiri ndipo lapulumuka mu mikwingwirima yambiri. Sitikufuna kukhala anthu ongokhalira kuchita mantha kapenanso kusalabadira za kuopsa kwa kachilombo ka corona kamene kali pakati pathu. Tiyeni tipemphere kuti Ambuye atembenuze mazunzo awa kuti akhale chimwemwe ndiponso kuti awadzutsa anthu ku zinthu zauzimu zimene samaziganizira.

Tiyeni tipitirire kupemphererana wina ndi mnzake ndipo tiyandikire kwa Ambuye. Mulungu akutiwerengera tonsefe kuti tikhale msanamira zokhulupirika za mu mpingo ndipo tikhale asilikali odalirika a mtanda wa Khristu amene tidzachirimika ndi kusasunthika ngakhale tili mkati mwa nsautso. Ambuye akudalitseni inu abale ndi alongo anga.

Ndimakukondani ndipo ndimakupemphererani,

Michael W. Smith

April 2020

"YANG'ANIRANI MBALAME ZA KUMWAMBA,
KUTI SIZIMAFESA AI, KAPENA SIZIMATUTIRA M'NKHOKWE;
NDIPO ATATE WANU WA KUMWAMBA AZIDYETSA.
NANGA INU MULIBE KUSIYANA NAZO KUZIPOSA KODI?"

MATEYU 6:26



Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone makalata akale.



CHITONTHOZO MU MALONJEZANO

M'BALE VALERI GLAAS (GERMANY)



Ngakhale kuti dziko lonse lili kakasi, kusowa pogwira, ambiri amwalira ndipo zinthu zimene zichitike mpaka kukwaniritsidwa kwa nthawi, Mulungu adzakhalabe thandizo la anthu ake maka kwa iwo amene ali oyera mu mtima mwao.

“Likatha thupi langa ndi mtima wanga, Mulungu ndiye thanthwe la mtima wanga, ndi cholandira changa chosatha. Koma ine, kundikomera kuyandikiza kwa Mulungu. Ndimuyesa Ambuye Yehova pothawirapo ine, kuti ndifotokozere ntchito zanu zonse.” (Masalmo 73:26, 28).

Pali malonjezano ambiri mu Masalmo 91 amene tikhoza kuwagwiritsa ntchito pa masautso amene tili nawo. Ngwodala iye amene adalira mwa Ambuye nadzilengezera malonjezanowa pa iye mwini. Mulungu wamphamvuzonse analonjeza kuti adzakhalabe chitetezo chatu ndi chishango chatu mu nthawi ya kusowa, ya mliri ndi matenda, ndipo ndife otetezeka ngati tikhazikika pa malonjezano akewo.

“Pakuti monga mawerengedwe a malonjezano a Mulungu ali mwa Iye eya; chifukwa chakenso ali mwa Iye Amen, kwa ulemerero wa Mulungu mwa ife” (2 Akorinto 1:20).

Taonani ulemerero umene tili nawo kuti tikhoza kusungana mtendere wa Mulungu mumtima mwathu mu nthawi zamsautso ndipo tikhoza kuwongoleredwa ndi nyimbo za maamboledwe.

“Inu ndinu mobisalira mwanga; m’nsautso mudzandisunga; mudzandizinga ndi nyimbo za chipulumutso” (Masalmo 32:7). Ambuye adalitse wina aliyense amene chiyembekezo chake chili mwa Yehova. Mulungu akudzadzeni inu ndi mphamvu komanso kulimba mtima kuti mukhoza kupembedza Ambuye ndi kumuyamika Iye ngati mu nyengo ngati izi.

“Koma ndidzakondwera mwa Yehova, ndidzasekerera mwa Mulungu wachipulumutso changa.” (Habakuku 3:18).

ZOKHUDZANA NDI MLIRIWU

M'BALE CHINWENDU NWACHUKWU (NIGERIA)



Nzodabwitsa kuti dzikoli likukumana ndi nthenda ina yoopsa imene ngati Ambuye satichitira chifundo, miyoyo ya anthu ambiri itaika.

Pokhala ana a Mulungu, tayitanidwa kuti tipereke zopempha zathu kwa Mulungu mu nthawi ngati izi. Ngakhale kuti pali zokambakamba zambiri zokhudza gwero la nthendayi, kuti kodi ndi yachilengedwe kapena anthu anachita kuipanga, pali chinthu chimodzi chimene sitingachisutse, chakuti Ambuye wailolera. Sabata zingapo zapitazo nthendayi isanafale, maganizo anga anatsogozedwa pa lembe limene liri pa Ezekiele 14:12-20.

“Ndipo anandidzera mau a Yehova akuti, Likandichimwira dziko ndi kuchita monyenga, ndipo ndikalitambasulira dzanja langa, ndi kulithyolera mchirikizo wake, ...Kapena ndikatumizira dzikolo mliri, ndi kulitsanulira ukali wanga ndi mwazi, kulidulira munthu ndi nyama; chinkana Nowa, Daniele, ndi Yobu, akadakhala m’mwemo, Pali Ine, ati Ambuye Yehova, sakadapulumutsa ana amuna kapena akazi; akadapulumutsa moyo wao wokha ndi chilungamo chao..”

Chimenechi chikuyenera kupangitsa kuti mu mtima mwanga mukhale katundu wolemera wakuti ndimutule pamaso pa Yehova. M'mene nthendayi ikuthamangira kufala kwake komanso kuti maiko akukanika kuigonjetsa zikungoonetseratu kuti munthu ndiolephera ngakhale samafuna kuvomereza. Izi zapangitsa kuti anthu adzichita mantha ndipo mitima isungunuke, koma ifeyo pemphero lathu ndiko lakuti Ambuye atithandize ndipo monga waitana ambiri kuti “akweze maso awo” malingana ndi zomwe analumulirira pa Luka 21: 25-28, popeza “chipulumutso chatu chayandikira.”

MU NTHAWI NGATI IZI

M'BALE BARTH NWACHUKWU (NIGERIA)



“Ndikweza maso anga kumapiri: Thandizo langa lidzera kuti? Thandizo langa lidzera kwa Yehova, wakulenga zakumwamba ndi dziko lapansi. Sadzalola phazi lako literereke: Iye amene akusungana sadzaodzera. Taonani, wakusungana Israele sadzaodzera kapena kugona” (Salmo 121:1-3).

Pamene ana a Israele anavutika ndi mliri mchipululu muja pomwe amalumidwa ndi njoka zamoto, iwo analirira kwa Mulungu kuti awathandize. “Pamenepo Yehova anati kwa Mose, Upange njoka ya moto, nuuike pa mtengo wake; ndipo kudzali, kuti onse olumwa, akuipenya njokayo, adzakhalabe ndi moyo” (Numenti 21:8). Ambuye Yesu Khristu anatilibikitsa ife ndi chitsanzo chomwecho. “Ndipo monga Mose anakweza njoka m’chipululu, chotero Mwana wa Munthu ayenera kukwezedwa; kuti yense wakukhulupirira akhale nao moyo wosatha mwa Iye” (Yohane 3:14-15).

Tikhale ndi chitsimikizo chakuti tili ndi Atate amene amakonda ana ake mu nyengo iliyonse. Ndipo mu nthawi ngati iyi, anthu paliponsepo apemphere “ndi kukweza manja oyera” kwa Mulungu amene amayankha mapemphero.

Dzukani ndi Kupemphera



M'BALE PETER AKWEYONA (KENYA)

Pena paliponse ku Kenya anthu akukhala mwa mantha, osadziwa chimene chiwachitikire tsiku linalo. Tsiku ndi tsiku zinthu zikutsekedwa, ngakhale malo opempherera, pofuna kuti mliriwu usafale. Ambuye akugwiritsa ntchito kachilomboka pofuna kuti olemera ndi osauka omwe onse abwere ku kulapa. Panthawi imeneyi, oyera mtima padziko lonse asaope koma adzuke napemphere kwambiri kuti Satana adzudzulidwe. Kudzera mu mwazi wa Yesu Khristu, ifeyo tachiritsidwa.

Tiyeni tione mavesi ochokera mu Baibulo amene amatitonthoza. “Pakuti Ine Yehova Mulungu wako ndidzagwira dzanja lako lamanja, ndi kunena kwa iwe, Usaope ndidzakuthandiza iwe.” (Yesaya 41:13). Ngakhale pali chiopsezo cha kudwala komanso imfa imene, komatu pali machiritso akumwamba. Chimenechi ndicho chifukwa chomwe a mpingo wa Church of God

akuyenera kukhala ndi nthawi ya kusala kudya ndiponso kupempherera oyera mtima padziko lonse lapansi. Mulungu wakonzera yankho la msautsowu ndipo ali chile ndi wokonzeka kuti apulumutse mtundu wa anthu. Chifukwa cha ichi, oyera mtima sakuyenera kukhala mwa mantha.

Pa Machitidwe 27:22, Paulo analankhula mkati mwa namondwe wamkulu panyanja kuti: “Koma tsopano ndikuchenjezani mulimbike mtima; pakuti sadzatayika wamoyo mmodzi mwa inu, koma ngalawa ndiyo.” Tikudziwa kuti m'maiko mwina miyoyo idzataika, koma mwa Ambuye muli moyo kuseli kwa imfa. Kwa okhulupirira onse, ino ndi nthawi yathu kuti tidzuke...tikhale maso ndipo tipemphere kuti nthenda yoopsayi ithe mu dzina la Yesu.

Mulungu adalitse dzikoli, oyera mtima ake onse, komanso ntchito ya uthenga wabwino. Mu dzina la Yesu, takupempherani. Amen.

“NDIKATSEKA KUMWAMBA KUTI PASAKHALE MVULA, KAPENA
NDIKALAMULIRA DZOMBE LITHE ZA PADZIKO, KAPENA
NDIKATUMIZA MLIRI MWA ANTHU ANGA; NDIPO ANTHU ANGA
OTCHEDWA DZINA LANGA AKADZICHEPETSА, NAKAPEMPHERA,
NAKAFUNA NKHOPE YANGA, NAKATEMBENUKA KULEKA
NJIRA ZAO ZOIPA; PAMENEPO NDIDZAMVERA M'MWAMBA, NDI
KUKHULULUKIRA CHOIPA CHAO, NDI KUCHIRITSA DZIKO LAO.”

— 2 MBIRI 7:13-14

M'BALE SHAHZAD BABAR (PAKISTAN)



Mzimu Woyera wabweretsa m'malingaliro mwanga lemba ili lochokera pa 2 Mbiri 7:14. Nkofunika kupitirira kusala kudya ndi kupemphera. Izi ndi zida zazikulu. Tikuyenera

kukhala omvera Mau a Mulungu, ndipo tikuyenera kuti tisaope koma tikhulupirire.

Tikupempha Ambuye kuti mwazi wake woyera ukhale pa ife tonse ndipo utiteteze. Ambuye akutetezeni mu dzina la Yesu. Amen.

Moni kwa oyera mtima a mu mpingo wa Church of God.

M'BALE MASTER GUSTOR (MALAWI)



Ndikukulemberani inu nonse ku dziko lonse lapansi, pamene maiko ena akuvutika ndi mliri uwu wa COVID-19. Ifeyo pokhala Akhristu tikuyenera kupemphera kwambiri mwa chikhulupiriro monga amanenera Malemba ku 2 Mbiri 7:13-14. Ndipo sitikuyenera kutopa mu masiku awa otsiriza.

Mulungu atichitira chokoma. Kumbukirani kuti Davide anapambana nkondo yomenyana ndi Goliati pamene anadalira Mulungu. Kumbukirani kuti chilichonse chimene munthu sangakwanitse kuchita, Mulungu adzachichita.

Chonde, inu Akhristu padziko lonse lapansi, tiyanjane limodzi ndi kupempherera mliri wa coronavirus. Mulungu adzayankha mapemphero athu. Mulungu adalitse maiko athu.

KODI CHIKHULUPIRIRO CHATHU CHILI KUTI?

M'BALE IVAN ECK (KANSAS, USA)



Tikudziwa kuti anthu ambiri ali ndi mafunso okhudza mliri uwu umene wafala padziko lonse womwe tikulimbana nawo. Ngakhale kuti pali zolinga zabwino zakuti ifeyo tichite zinthu mosamalitsa ndithu, Mulungu sangafune kuti mitima yathu ikhale yopsinjidwa komanso kusautsika

chifukwa cha mantha amene tili nawo. Choncho, tifunsane funso ili, “Kodi tichite chiyani m'nyengo zino zimene sitikudziwa kuti chibwere mawa nchiyani?”

Baibulo liri ndi zitsanzo zochuluka za anthu oopa Mulungu amene anakumana ndi nyengo zochititsa mantha pa moyo wao. Komabe mu nthawi zoopsazo, iwo anaphunzira kudalira mwa Mulungu wa kumwamba. Pamene tikuyang'ana m'mbuyo ndikumaona zitsanzo zonse za m'mene Mulungu anathandizira anthu ake, tikuyenera kukhala ndi nthawi yachete yoyang'ana kwa Mulungu ndi kukhala olimbika mtima!

Timapeza malangizo ena abwino mu mutu 12 wa kalata ya kwa Ahebri. Akutiuzwa kuti titaye cholemetsa chilichonse komanso zinthu zauchimo. Zimenezi zikhoza kutilepheretsa ife kuti tisapambane pa moyo wathu wauzimu. Tsono, pamene tikuthamanga mwa chipiriro pa mpikisanowo umene waikidwa patsogolo pathu, tiyeni tiyang'ane kwa Yesu amene ali woyamba ndi wotsiriza wa chikhulupiriro chathu!

Ndikutsimikizika kuti Ambuye analola kuti tikumane ndi mavuto ngati awa kuti potero mizimu yathu itsitsimuke ndi kumukhulupirira Mulungu koposa kale. Wolemba Salmo anati, “Tsiku lakuopa ine, ndidzakhulupirira Inu.” (Salmo 56:3), ndipo kenaka anatinso, “Pamene munati, Funani nkhope yanga; mtima wanga unati kwa Inu. Nkhope yanu, Yehova, ndidzaifuna.” (Salmo 27:8).

Oyera mtima, limbikitsidwani! Ndikudziwa kuti Muomboli wanga ali ndi moyo! Mtsogoleri wa chipulumutso chathu ndiye mphamvu yomweyo imene inatsekula njira kuti pa Nyanja Yofiira! Iye ndi amene anatsekula maso a akhungu

NYENGO ZOSAUTSA

M'BALE W. S. VEDHA (INDIA)



Ine ndi ndi zaka zakubadwa pafupifupi 65 ndipo pamoyo wanga ndakumana ndi nyengo zovuta zosiyanasiyana mu moyo wanga wachikhristu. Mliri uwu wa coronavirus watiphunzitsa ife zinthu zambiri mu miyezi iwiri iyi imene yapita. Tikupemphera kwa Ambuye ndi kumafunsa kuti, “Kodi kumeneku ndiko kumapeto kwa nthawi komanso kubweranso kwa Yesu?” [“Koma za tsiku ili ndi nthawi yake sadziwa munthu aliyense, angakhale angelo a Kumwamba, kapena Mwana, koma Atate yekha.” Mateyu 24:36.]

Mu zaka 45 zimene ndakhala ndikutumikira, sitinaphonyeko kupita ku tchalichi lamulungu ndi limodzi lomwe. Koma lamulungu lapitali, tinayimitsa kukumana chifukwa cha lamulo lochokera ku boma. Zimenezi zinali zopweteka kwambiri mu mtima mwanga.

Abale okondeka ndi oyera mtima, chonde pemphererani dziko la India. Iye tikupemphera chifukwa cha nyengo zoziyanasiyana pa dziko lonse lapansi. Mulungu wathu ndi wamphamvuzonse. Ndipo Iye amachita zodzabwitsa kwa ana ake. Amen.

komanso olumala anayenda nalumpha ndi chimwemwe! Motsimikiza mtima Iye anaima pamaso pa anthu akufa nawaitana kuti akhalenso ndi moyo! Iye anatonholetsa namondwe woopsa ndi Mau ake okha! Iye anachiritsa kwathunthu akhate amene analibe chiyembekezo! Iye anali ndi chifundo pa iwo amene anali wochimwa ndi wonyozedwa! Iye anadabwitsa anthu anzeru ndi mayankho ake! Iye anatulutsa mizimu yoipa mwa chikhamu ndipo anamumasula nakhalenso munthu wabwinobwino monga kale! Iye ndiye linga lathu ndi nsanja yathu! Iye ndiye mtsogoleri wathu ndipo sachita manyazi kutitchula ife kuti abale ake! Iye ali “bwenzi lopambana ndi mbale woumirira.” (Miyambo 18:24). Iye analimbana ndi mdierekezi mu chipululu ndipo anapambana! Iye anapita pamtanda ndipo anapereka moyo wake ngati chiombolo kwa anthu ochuluka! Iye analimbana ndi imfa ndipo anaichotsa ululu wake! Iye anapita kumanda ali wakufa ndipo anatulukako ali wamoyo! Iye anauka! Iye amapangitsa kuti nkondo ndi kukangana kusiyike! Iye ndiye Kalonga wa Mtendere! Iye ndiye wodalitsika ndi Mkhlapakati yekhayo! Iye ndiye Mfumu ya Mafumu komanso Mbuye wa Ambuye! Iye ndi Alefa ndi Omega! Iye ndi Mpulumutsi wanga!

Yoswa ndi ana a Israele anafika pa nyengo yakuti akuyenera kupanga chisankho. Yoswa anapereka yankho ili lomveka bwino, “koma ine, ndi a m'nyumba yanga, tidzatumikira Yehova.” (Yoswa 24:15).

Anzanga okondeka, ndikufunsi, “Kodi chikhulupiriro chanu chili kuti?”

Mulungu akuti yitana ife. Iye akufuna kuti ifeyo tigwiritse ntchito nthawi ngati izi kuti tidzifufuze moona mtima; ndipo izi zimatanthauza kuti ifeyo tidziwunike tokha, ngati tikadalidi mu chikhulupiriro. Kodi tabisala mu thanthwelo, limene lili Khristu Yesu?

Khalani olimbikitsidwa!

Mulungu adalitse wina aliyense!

MAGORIMISABIBU: CHOOPSA PAKATI PAKO

M'BALE JOHN VARGHESE (INDIA)



Pa Yeremiya 20:1-3 akunena kuti, “Ndipo Pasuri mwana wake wa Imeri wansembe, amene anali kapita wamkulu m’nyumba ya Yehova...anampanda Yeremiya mneneriyo, namuika matangadza... Ndipo Yeremiya anati kwa iye, Yehova sanatche dzina lako Pasuri, koma Magorimisabibu.”

[mantha kapena choopsa pakati pako].

Dziko lonse lapansi lili ndi mantha ndipo likuopsedwa ndi COVID-19. Nthendayi yatenga miyoyo ya anthu mazanamazana ndipo ambirinsu akuzunzika ndi kusautsika nayo. Atsogoleri a maiko aika mfundo zokhwima pofuna kugonjetsa ndi kupambana ka chilomboka komanso kupulumutsa miyoyo ya anthu.

Pamene Mulungu anatumiza miliri ku Egipto kudzera mwa Mose, amatsenga a mfumu Farao anayetsetsa kukopera ndi kuchitanso chimodzimidzi kuti agonjetse miliriyo, koma iwo anakanika. Pamapeto ake iwo anati, “Chala cha Mulungu ichi” (Eksodo 8:19). Pa nthawi ya Nowa, pamene Mulungu anaona kuti kuchimwa kwa anthu kunali kwakukulu pa dziko, Iye anaganiza zoononga dziko ndi chigumula (Genesis 6:5, 6). Chimodzimidzinsu, Mulungu

anaganiza zoononga Sodomu ndi moto poona zoipa zochulukira za anthu okhala kumeneko. Malingana ndi mneneri Ezekiele, poonjezera pa kugonana kwa amuna kapena akazi okhaokha, machimo ena a anthu a ku Sodomu anali kudzikuzi, kuchulukira kwa chakudya, kukonda kungokhala mtambasali kapena kungofuna zofewa nthawi zonse, ndi kupondereza osowa ndi osauka (Ezekiele 16:49). Yesu anati pa Luka 17:26-30 kuti monga zinaliri pa tsiku la Nowa ndi pa tsiku la Loti zidzakhalsu chimodzimidzi m’masiku a kubweranso kwa Mwana wa Munthu.

Ngakhale kuti miliri inabwera yochulukira, Mfumu Farao anaumitsabe mtima wake ndipo anafa. M’ malo moomitsa mtima wathu, tiyeni ngati dziko lonse tilape ndi kutembenukira kwa Mulungu kuti atichiritse kwathunthu osati ku kachilombo kokhaka komanso ku chilango cha uchimo.

Tiyeni tipemphere kwa Mulungu mpaka atatambasula dzanja lake la chifundo kwa mtundu wa anthu. Tiyeni tidziweruze tokha, tizindikire nyengo zimene tilimo, ndipo tiyang’anire miyoyo yathu. Ambuye wathu ali pa chipata ndipo posachedwapa abweranso kuti adzaweruze.

Chikhulupiriro osati Mantha

INU MULI MCHERE WA DZIKO LAPANSI

M'BALE PAUL PHILLIPS (CALIFORNIA, USA)



“Inu muli mchere wa dziko lapansi...” Kodi ndi kangati kamene mwakhala pansu ndi kulingalira za zimene zikuchitika lero m’dzikoli? Kodi mukuganizapo bwanji? Ndaona m’mene anthu nkhanayi akuyilandirira nkhanayi. Ena zochita zawo zikuonetsa kuti ali ndi mantha. Pamene

ena akuchita molingana ndi m’mene munthu amaganizira. Kodi mkhristuwe nkhanayi wayilandira bwanji? Ukuyiganizira motani? Kodi maganizo ako ndi a mtendere? Kodi uli ndi bata mkati mwako? Tikuyenera kukhala mdalitso: miyoyo yathu ikuyenera kukhala yopulumutsa ndi kuteteza dzikoli ku chionongeko ndi kuola kwathunthu.

Polingalira zimene ndazona, ndazindikira ichi—iyi si nthawi yochita mantha. Iyi ndi nthawi yakuti tikule. Nthawi yozindikira phindu la chipulumutso chenicheni, kupereka mtendere umene umaposa chidziwitso chonse, umene umatsamira pa chikondi cha kwa Mulungu chimene

chimathamangitsa mantha a chionongeko. Tapatsidwa malonjezano a Wamphamvuzonseyo! “Kodi ndi chiyandinso china chimene tinganene popeza zonse Iye wanena kale...” Mverani mau ake! Kodi chikhulupiriro chanu chili kuti? Nanga chiyembekezo chanu chili kuti? Nanga inuyo muli kuti? Kodi mwakhazikika pa zitizo? Mkati mwa anamondwe, timapeza zimene tili nazo kale komanso zimene timazisowa. Ndife odala kuima pamaso pa Mulungu chotere, kutionetsa zimene tili nazo mkati mwathu! Kodi sichinthu cha mtengo wapatali kudziwa pamene ife tili molingana ndi kuwala kwa Mau ake?

Ndili ndi lonjezo limene lalembedwa pa ma cheke anga akubanki kuti adzindikumbutsa komanso kuwalozera ena za mau oona a Wamphamvuzonseyo: Pakuti Yehova Mulungu ndiye dzuwa ndi chikopa; Yehova adzapatsa chifundo ndi ulemerero; sadzakaniza chokoma iwo akuyenda angwiro. Yehova wa makamu, wodala munthu wakukhulupirira Inu.” (Salmo 84:11-12).

KUTALIKIRANA POKHALA KAPENA KULUMIKIZANA KUUZIMU?



“Kutalikirana pokhala” ndi mau amene akugwiritsidwa ntchito pafupipafupi. Kumeneku ndiko kuwonetsesa kuti anthu akutalikirana kwa 1 metre poopa kuti akayandikana kwambiri akhoza kupatsirana kachilombo koyambitsa COVID-19. Anthu akuyenera kupewa kukhala m'malo m'mene mumapezeka chigulu cha anthu ndipo zimenezi zachititsa kuti maiko atseke mabizinesi ndi masukulu. Zotsatira zake ndi zakuti anthu ambiri tspano akukhala kumanyumba kwao ndipo sakumakumana ndi anzawo ngati kale komanso chiyanjano cha sabata iliyonse kapena mathandizo ochokera kwa anthu ena sakupezeka.

Imeneyi ndi nthawi yabwino ya “kulumikizana kuuzimu.” Choyamba, gwiritsani ntchito nthawi yopofuna kuti

mulumikizane kwambiri ndi Ambuye Yesu ndiponso kuti mulimbikitse ubale wanu ndi Mulungu. Chachiwiri, ngakhale kuti simungathe kukhala pamodzi ndi munthu wina, mukhoza kukhala mnzake wa munthu winayo. Mukhoza kumutumizira uthenga pa sms, kapena pa Whatsapp kapena kumuyimbira foni. Potoero mudzakuzana kulumikizana kwanu ndi anthu ena kuuzimu komanso kuwalozera iwo kwa Khristu. Pali anthu ambiri amene amadzimva kuti ali okhaokha, alibe mnzawo ndipo ali ndi mantha. Boma lanena kuti anthu atalikirane ndipo Ambuye akunena kuti tilumikizane kuuzimu. Mukhoza kusintha moyo wa munthu wina lero pokhala chilimbikitso kwa iye.

—mws

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org



**Mau a
Nyengo
Yake**

ZOVALA ZOPINDIDWA




M'BALE ED WILSON (OKLAHOMA, USA)

Mu nkhani ya kuukitsidwa kwa Yesu mu Yohane 20:6-8 timauzidwa kuti, “Pamenepo anadzanso Simoni Petro alikumtsata iye, nalowa m'manda; ndipo anaona nsalu zabafuta zitakhala, ndi mlezo, umene unali pamutu pake, wosakhala pamodzi ndi nsalu zabafuta, koma wopindika padera pamalo pena. Pamenepo tsono analowanso

wophunzira winayo (Yohane),...ndipo anaona, nakhulupirira..”

Yohane anafika ku manda amene Yesu munalibe ndipo anapeza zovala za Yesu zimene anamukulunga nazo zitapindidwa pamodzi bwino lomwe, ndipo mlezo umene unali kumutu kwake utaidikwa pena osati pamodzi ndi zovalazo. Nthawi yomweyo zonse zimene Yesu anakhala akuwauza onsewo zinamubwerera. Thupi lake sikuti linali litabedwa ayi. Imeneyi sikuti inali ntchito ya anthu oipa, ongofuno kuti ngakhale mu imfa akane zakuti amene amamukonda atonthozedwe pomuyandikira. Kapenanso siinali ntchito ya azinzake, popeza iwo sakananyoza thupi la m'bale amene amamukonda politenga lili lamaliseche. Ayi ndithu, munthu uja amene anakhala akumuona m'masiku omaliza a moyo wake, anadzichitira Iye mwini zomwe anachitanso kwa Lazaro pamene analamulira kuti amumasule nsalu zake zakumanda zimene anamukulunga nazo.



Kapenanso sanatuluke monga munthu amene anali wakuti wakomoka ndipo atatsitsimuka, maganizo nkubwerera mchimake, anazindikira zomwe zamuchitikira nkuyamba kuthawa. Mwabata komanso mwadaladala pofuna kuonetsa mphamvu ya umbuye wake pa imfa ndiponso kuti samalabadira za asilikali olondera pamanda aja kapena Afarisi, Iye anauka kuchokera pamene anagona ndipo pochoka anasamala bwino pamalo pamene panali chisokonezo. Zimene Yohane anachita atazindikira tanthauzo la zovala zopindidwazo angozinena kuti “anakhulupirira.” Imeneyi inali nsonga yofunikira mu kukula kwa chikhulupiriro chake, ndipo iye anafulumuzidwa ndi Mzimu wa Mulungu kuti zimenezi azilembe kuti potero inuyo ndi ineyo tipindulepo.

CHIYERO CHA KWA AMBUYE